# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA KARONGA M'DZINJA LA 2024-2025

## Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 mwachidule

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.


Boma la Karonga likuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo mu nyengo ya mvula ya 2025/2026.

## October 2025




Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula mu mweziwu.
Komabe pali kuthekera kodzalandila mvula ya Chizimalupsya yomwe idzakhale ya mphepo ya mkuntho ndi mphezi m'madera ena.


## November 2025




M'Bomali tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika.

Madera ambiri akhoza kudzalandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm yomwe idzakhale ya mphezi ndi mphepo ya mkuntho.


## December 2025




Mu December, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okhazikika wa pakati pa 100mm ndi 200mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka m'sabata lachitatu mweziwu

## January 2026





Mwezi wa January ukuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo okazikika kapena kuposera apo.

Madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm.


Ng'amba ya masabata awiri ikuyembekezeka mu mweziwu.

## February 2026




Mlingo wa mvula okhazikika kapena kuposera apo ukuyembekezeka m'madera ambiri. Mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezeka madera ambiri.
Pali chiopsezo cha ng'amba ya masabata awiri mu mweziwu.

## March 2026





Mu March, mvula ya mlingo oposa 200mm ikuyembekezeka madera ena.

Mvula ya mlingo ochulukirapo ikuyembekezeka m'madera ambiri a kwa T/A Kyungu.

Chiopsyezo cha ng'amba yokwanila sabata limodzi ikuyembekezeka.

## April 2026





Mu mweziwu, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm.
Karonga Boma komanso madera ena ozungulila akuyembekezeka kulandila mvula yoposera 250mm.

Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa April.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kugwa kuyambira sabata lachitatu la mwezi wa December 2025. Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa April chaka cha 2026.Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kukhala yotalika masiku a pakati pa 130 ndi 140. Pali chiopsezo chachikulu cha ng'amba ya ma sabata awiri mu mwezi wa January ndi February n'chaka cha 2026.

| KARONGA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.0 | 0.0 | 5.0 |
| NOV | 6.5 | 56.8 | 34.9 |
| DEC | 101.7 | 178.2 | 137.2 |
| JAN | 135.9 | 214.3 | 191.8 |
| FEB | 113.4 | 154.0 | 132.8 |
| MAR | 159.5 | 266.4 | 208.3 |
| APR | 80.8 | 184.4 | 245.7 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu mwezi wa December 2025**
**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zapangidwa ndi kusindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: